# PHUNZIRO LA 22

1. Kodi Mulungu amkakudziŵa kuchimwa kwa anthu a ku Sodomu ndi Gomora?
-Inde.

2. Kodi anthu akayiwala za Mulungu, Mulungu amaŵayiwa-la iwowo?
-Iyayi.

3. Kodi anthu akayiwala za Mulungu, Mulungu amayiwala za machimo awo?
-Iyayi.

4. Kodi chifukwa chiyani Mulungu akuyenera kupereka chilango pa tchimo lililonse?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wabwino kwambiri.
-Chifukwa chakuti Mulungu anaŵalenga anthu ali abwino kwambiri.
-Chifukwa chakuti tchimo lililonse limatsutsana ndi Mulungu.

5. Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanangofikira kupereka chilango kwa anthu a ku Sodomu ndi Gomora chifukwa cha machimo awo?
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti anthu a ku Sodo-mu ndi Gomora alape machimo awo.
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti aŵapulumutse anthu a ku Sodomu ndi Gomora.

6. Kodi chifukwa chiyani Mulungu sakufuna kungofikira ku-pereka chilango kwa anthu chifukwa cha machimo awo lero lino?
-Chifukwa chakuti Mulungu akufuna kuti anthu tilape machimo awo.
-Chifukwa chakuti Mulungu akufuna kutipulumutsa.

7. Kodi Mulungu amangofuna kuwawopsyeza anthu, koma

asaŵapatsa chilango chifukwa cha machimo awo?
-Iyayi.
-Mulungu adzapereka chilango pa machimo onse.

8. Kodi nthaŵI ikadzakwana yakuti Mulungu apereke chilango kwa nthu ochimwa, pali amene angadzathe kumuletsa Iye?
-Palibe.

9. Ngati m'mene tchimo limkamuŵandikitsirabe Loti ku Sodomu, kodi tchimo limachita chiyani kwa anthu a masiku ano?
-Tchimo limaŵandikitsirabe anthu ku kuyipa kwake.

10. Kodi anthu a masiku ano akufanana ndi anthu a ku Sodomu ndi Gomora?
-Inde.

11. Kodi anthu a masiku ano akufanana bwanji ndi anthu a m'mizinda ya Sodomu ndi Gomora?
-Anthu a masiku ano timanama kwambiri.
-Anthu a masiku ano takhala tikuŵanamizira anthu ena zinthu zambiri.
-Anthu a masiku ano takhala tikuŵatembelera abale athu.
-Anthu a masiku ano takhala tikuba zinthu zambiri za anthu ena.
-Anthu a masiku ano takhala tikugona ndi akazi a amuna ena.
Anthu a masiku ano takhala tikuŵapha anthu ena.

12. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamupulumutsa Loti?
-Chifukwa chakuti Loti amkadziwa kuti anamuchimwira Mulungu.
-Chifukwa chakuti Loti amkadziwa kuti tchimo lake lidzamubweretsera imfa yosatha.
-Chifukwa chakuti Loti amkadziwa kuti Mulungu yekha ndi amene angathe kumupulumutsa iye.

-Chifukwa chakuti Loti amkakhulupilira kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi kudzamupulumutsa iye.

13. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamusandutsa mkazi wa Loti mwala wa mchere?
-Chifukwa chakuti mkazi wa Loti sanamumvere Mulungu, ndipo anachewukira m'mbuyo.

14. Kodi chifukwa chiyani mkazi wa Loti anachewukira m'buyo?
-Chifukwa chake amkaŵakonda machimo ake.
-Chifukwa chakuti samkafuna kuti aŵasiye machimo ake.

-Mulungu analonjeza zakuti adzamupatsa Adamu ndi Hava mwana wa mamuna.

-Abulahamu anali ndi zaka 100, ndipo Sala anali ndi zaka 90, koma analibe ana.

-Kodi Mulungu anayiwala lonjezo Lake lomupatsa Abulahamu mwana wa mamuna?
-Iyayi.

-Mulungu sangayiwale malonjezo Ake.
-Mulungu amasunga malonjezo Ake.

-Kodi Mulungu anasintha maganizo Ake omupatsa Abulahamu mwana wa mamuna?
-Iyayi.

-Mulungu sangasinthe maganizo Ake.
-NthaŵI zonse Mulungu amachita chimene walankhula kuti achichita.

-Abulahamu anali ndi zaka 100, ndipo Sara anali ndi zaka 90 ndipo anali osabereka.

-Kodi kunali kovuta kwa Mulungu kuti amupatse Abulahamu ndi Sara mwana wa mamuna?
-Iyayi.
-Palibe chomuvuta Mulungu.
-Mulungu akhoza kuchita china chilichonse.

-Ngati m'mene Mulungu analonjezera, Iye anamupatsa Abulahamu ndi Sara mwana wa mamuna.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 21:1-3

1-AMBUYE anamukumbukira Sara ndipo anamuchitira chimene anamulonjeza.
2-Chomcho Sara anatenga pathupi, namuberekera Abulahamu mwana wa mamuna pamene Abulahamuyo anali okalamba. Mwana ameneyu anabadwa pa nthaŵI yeniyeni yimene Mulungu adanena.
3-Ndipo mwana wa Abulahamuyo, mwana amene sara anamuberekerayo, Abulahamu anamutcha kuti Isaki.

-Kodi zanatheka bwanji Abulahamu, amene anali ndi zaka 100, ndi Sara amene anali ndi zaka 90 ndipo osabereka, kukhala ndi mwana wamamuna?

-Chifukwa chakuti ndi Mulungu amene amapereka moyo.
-Chifukwa chakuti Mulungu angathe kuchita china chilichonse.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene amapereka moyo kwa anthu onse.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene amapereka moyo kwa ana anu onse.

-Chifukwa chakuti ndi Mulungu amene ankapereka moyo kwa makolo anu onse.
-Chifukwa chakuti ndi Mulungu amene amapereka moyo kwa anthu onse kwina kulikonse.

-Anali Mulungu amene anapereka mwana wa mamuna kwa Abulahamu ndi Sara.
-Abulahamu anamutcha mwanayo dzina lakuti Isaki.

-Patatha zaka zambiri, Isaki anakula kukhala mnyamata.
-Abulahamu ndi Sara amkamukonda Isaki kwambiri.

-Kodi Abulahamu ndi sara amkadziwa zakuti Mulungu anakonza zotumiza Mpulumutsi kupitira mu m'bado wa Isaki?
-Inde.

-Abulahamu ndi Sara anakumbukira kuti Mulungu analonjeza zodzatumiza Mpulumutsi kupitira mu m'bado wa Isaki.

-Tsiku lina Mulungu analankhula za Isaki kwa Abulahamu.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 22:1-2

1-Pambuyo pake Mulungu anamuyesa Abulahamu. Anamuyitana, anati, "Abulahamu,!"Ndipo Abulahamu anayankha, "Ndili Pano."
2-Kenako Mulungu anati, "Tenga Isaki mwana wako m'modzi yekha amene umamkonda kwambiri uja, upite ku dziko la Moliya. Kumeneko ukampereke ngati msembe yopsereza pa phiri limene ndidzakuwuza."

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamulamula Abulahamu kuti amupereke Isaki ngati msembe yopsereza?
-Mulungu amkafuna kuti awone ngati Abulahamu amkamukonda Mulunguyo kwambiri kuposa Isaki.

-Kodi zinatheka bwanji kuti Mulungu amulamule Abulahamu kuti amupereke Isaki ngati msembe yopsereza?

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anamupatsa moyo Abulahamu.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anamupatsa moyo Isaki.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi AMBUYEwa anthu onse.

-Kodi anasi anu angaŵawuze ana anu zochita?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti anasi anu si ambuye  a ana anu.

-Kodi anasi anu angakulamuleni m’mene mungadzalire mbewu m’munda mwanu?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti anasi anu si mbuye wa munda wanu.

-Kodi AMBUYE a Isaki ndi ndani?
-Mulungu.

Kodi AMBUYE a anthu onse ndi ndani?
-Mulungu.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi AMBUYE a anthu onse, Mulungu ndi amene angathe kuŵalamula anthu onse chimene Iye akuchifuna.

-Kodi Abulahamu anachita chiyani Mulungu atamulamula kuti amupereke Isaki ngati msembe?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 22:3

3-M’mawa mwake, Abulahamu anakonza chokhalira pa bulu wake nadulanso nkhuni zokawotchera msembe, ndipo anamutenga Isaki pamodzi ndi antchito ake aŵiri, nanyamuka ulendo opita ku malo amene Mulungu anamuwuza.

-Abulahamu anadula mkhuni zowotchera msembe, ndipo anatenga Isaki ndi antchito ake aŵiri, ndipo anapita ku malo kumene Mulungu anamuwuza.

-Kodi Abulahamu anakampereka bwanji Isaki ngati msembe?

-Kodi Abulahamu anakampereka Isaki ngati msembe, Mulungu anakakwanilitsa bwanji malonjezo Ake?

-Kodi Abulahamu anakamupereka Isaki ngati msembe, Mulungu anakamupatsa bwanji Abulahamu zidzukulu zambiri?

-Kodi Abulahamu anakamupereka Isaki ngati msembe, Mulungu anakamutumiza bwanji Mpulumutsi ngati chidzukulu cha Abulahamu?

-Kodi Mulungu anasintha maganizo Ake?
-Kodi Mulungu anaganiza zophwanya lonjezo Lake?

-Kodi Mulungu anasintha zomupatsa Abulahamu zidzukulu zambiri?
-Kodi Mulungu anasintha maganizo Ake otumiza Mpulumutsi kuti adzaŵapulumutse anthu.

-Kodi Abulahamu anakamupereka bwanji Isaki ngati msembe?
-Kodi mukuganiza kuti Abulahamu amkaganiza kuti Mulungu anasintha maganizo Ake?
-Iyayi.

-Abulahamu amkakhulupilira mwa Mulungu ndi malonjezo Ake.
-Abulahamu amkakhulupilira kuti Mulungu adzasunga malonjezo Ake.

-Abulahamu amkakhulupilira kuti Mulungu amkasunga pangano Lake lomupatsa iye zidzukulu zambiri.

-Abulahamu amkakhulupilira kuti Mulungu adzasunga pangano Lake lotumiza Mpulumutsi.

-Abulahamu amkakhulupilira kuti akamupereka Isaki ngati msembe, Mulungu adzamudzutsa Isakiyo kuchokera kwa akufa.

-Abulahamu anali osiyana ndi Adamu ndi Hava.

-M'munda wa Edeni, Mulungu anamuwuza Adamu ndi Hava kuti adzafa akadzadya chipatso kuchokera mu Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa.

-Adamu ndi Hava sanamukhulupilire Mulungu.
-Koma Abulahamu anamukhulupilira Mulungu.

-Chifukwa chakuti Abulahamu anamukhulupilira Mulungu, anatenga Isaki ndi antchito ake aŵiri kupita nawo ku malo amene Mulungu anakaŵalozera.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 22:4-6a

4-Pa tsiku lachitatu lake, Abulahamu anawawona malowo chapatali.
5-Ndipo anawawuza anthito ake aja kuti, "Inu bakhalani pano ndi buluyu. Ine ndi mnyamatayu tipita uko kukapephera, tidzakupezani pambuyo pake."
6-Abulahamu anamusenzetsa Isaki nkhuni zokawotchera msembe yopsereza ija, iyeyo anatenga moto m'manja mwake, pamodzi ndi mpeni.

-Abulahamu ndi Isaki akuyendera limodzi, Isaki anawafunsa bambo ake.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 22:6b-7

6-Aŵiriwo akuyendera limodzi,
7-Isaki anaŵayitana bambo ake kuti, “Atate. “ Abulahamu anavomera kuti, “Ee, mwana wanga.” Isaki anafunsa kuti, “Moto ndi nkhuni ndikuziwona, zilipo, koma nanga mwana wa nkhosa wokawotchera msembe ali kuti?”

-Kodi funso la Isaki linali lotani?
-“Kodi mwana wa nkhosa wokawotchera msembe ali kuti?”

-Isaki amkadziwa kuti atate ake amkapita kukapereka msembe.
-Isaki amkadziwa kuti anatenga moto ndi nkhuni.

-Koma Isaki samkamvetsa chifukwa chimene iwowo sanatengele mwana wa nkhosa.

-Kodi Abulahamu anayankha chiyani kwa Isaki.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi22:8

8-Abulahamu anayankha, “Mwana wanga, Mulungu Mwini akatipatsa mwana wa nkhosayo.” Chomcho aŵiriwo anapitiliza ulendo wawo limodi.

-Kodi Abulahamu anayankha chiyani?
-Abulahamu anayankha kuti Mulungu Mwini akaŵapatsa mwana wa nkhosayo.

-Abulahamu amkakhulupilira kuti Mulungu akapereka msembeyo.

-Kukhulupilira mwa Mulungu ndi tchito yofunika kwambiri kuti tidziyichita.

-Kumangomvera uthenga wa Mulungu kokha sikungathe kutipulumutsa ife.
-Tiyenere kumakhulupilira mawu a Mulungu kuti tidzapulumutsidwe.

-Apa pali chitsanzo:

-Munthu amene amkadwala anapita kwa dokotala.
-Dokotala uja anamuwona munthu odwala uja ndipo anamuwuza za matenda amene ankadwalawo.

-Kenako dokotala uja anapereka mankhwala kwa munthu odwala uja kuti akhalenso bwino.

-Munthu odwala uja anangotenga mankhwalawo ndikuŵasunga nthumba mwake ndikumabwerera ku nyumba kwakwe.

-Koma munthu odwalayo sanamwenso mankhwalawo.
-Munthu odwalayo anangomvera zimene analankhula dokotala uja koma sanamwe mankhwalawo.

-Kodi munthu odwalayo anachila?
-Iyayi.

-Kumangomvera mawu a Mulungu kokha, sikungakupulumutseni inu.
-Muyenera kumakhulupilira mawu a Mulungu ngati Abulahamu.
-Mumangomvera mawu a Mulungu, koma osakhulupilira, ndipo muli ngati Satana.

-Ngati mukungomvera mawu a Mulungu koma osakhulupilira, ndiye kuti mukumutcha Mulungu kuti ndi wabodza.

-Mulungu amaŵapulumutsa anthu okhawo amene amakhulupilira mwa Iye.

-Mulungu amaŵapulumutsa anthu okhawo amene ama-
khulupilira mawu Ake.

-Kodi mawu a Mulungu ali kuti?
-M'buku la Mulungu, Bayibulo.

-Abulahamu ndi Isaki atafika pa malo amene Mulungu anaŵalozera, kodi chinachitika ndi chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 22:9-10

9-Atafika ku malo amene anamuwuza Mulungu aja, Abulahamu anamanga guwa nayika nkhuni pamwamba pa guwalo. Kenako adamanga mwana wake uja, namugoneka pamwamba pa nkhunizo.

10-Kenako anasolola mpeni kuti amuphe mwana wakeyo.

-Kodi Abulahamu anachita chiyani?
-Anam'manga Isaki ndikumugoneka pamwamba pa guwa.

-Kodi Abulahamu anakatha kumupulumutsa Isaki?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani Abulahamu sanakatha kumupu-
lumutsa Isaki?
-Chifukwa chakuti Abulahamu anali atanyamula kale dzanja lake kuti amuphe Isaki ndikumupereka ngati msembe.

-Kodi Isaki anakatha kudzipulumutsa yekha?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani Isaki sanakatha kudzipulumutsa yekha?
-Chifukwa chakuti Abulahamu anamanga manja ndi miyen-
do ya Isaki.

-Panalibe njira yopulumukira Isaki.
-Panalibe njira yakuti anthu amene anaŵatsekera kunja kwa chombo chija apulumukire ku chigumula chimene Mulungu anachitumiza.

-Panalibe njira yakuti anthu a ku Sodomu ndi Gomora apulumukire ku moto umene Mulungu anawutumiza kuchokera kumwamba.

-Panalibe njira yakuti mkazi wake wa Loti anakapulumukira atayang'ana m'mbuyo ku mzinda wa Sodomu.

-Abulahamu sanakatha kumupulumutsa Isaki
.-Isaki sanakatha kudzipulumutsa yekha.

-Kodi ndani yekha amene anakatha kumupulumutsa isaki?
-Mulungu.

-Anthu ena sangathe kutipulumutsa ife.
-Ife sitingathe kudzipulumutsa tokha.

-Kodi ndani yekha amene angathe kutipulumutsa ife?
-Mulungu.

-Mulungu yekha ndi amene anamupulumutsa Nowa ndi banja lake.

-Mulungu yekha ndi amene anamupulumutsa Loti ndi ana ake akazi aŵili.

-Mulungu yekha ndi amene angathe kupulumutsa anthu onse.
-Mulungu yekha ndi amene anakatha kumupulumutsa isaki.

-Kodi Mulungu anamupulumutsa Isaki?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 22:11-12

11-Koma mngelo wa AMBUYE anamuyitana kuchokera kumwamba, anati, “Abulahamu, Abulahamu!” Iye anayankha kuti, “Ee, AMBUYE!” Mngeloyo anati,

12-“Usamuphe mnyamatayo, kapena kumuchita kanthu kena kalikonse. Tsopano ndadziwa kuti iwe ndiwomveradi Mulungu, chifukwa chakuti siwunandimane mwana wako m’modzi yekhayo.”

-Kodi ndani amene analankhula kwa Abulahamu ndukumupulumutsa Isaki?
-Mulungu.

-Mulungu yekha ndi amene anatha kumupangitsa Abulahamu kuti asamuphe Isaki.
-Mulungu yekha ndi amene anatha kumupulumutsa Isaki.

-Koma Isaki sanakapulumutsidwa panakakhala kuti panalibe msembe yina.

-Kodi Abulahamu anali ndi msembe yina?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 22:13

13-Abulahamu atayang’ana, anawona kuti pali nkhosa ya mphongo yimene yinakodwa ndi nyanga zake mu ziyangoyango. Anapita kukayigwira, nayipha ngati msembe yopsereza m’malo mwa mwana wake uja.

-Isaki analibe msembe ina iliyonse.
-Abulahamu analibenso msembe ina iliyonse.

-Kodi ndani amene anapereka msembe yolowa m’malo mwa Isaki?

-Mulungu.
-Mulungu yekha ndi amene anapereka msembeyo.

-Kodi msembe yimene Mulungu naperekayo yinali chiyani?
-Mwana wa mphongo wa nkhosa.

-Kodi mwana wa mphongo wa nkhosayo anali kuti?
-Anakodwa ndi nyanga zake mu ziyangoyango.

-Kodi chifukwa chiyani mwana wa nkhosayo anakodwa ndi nyanga zake mu ziyangoyango?
-Chifukwa chakuti Mulungu anamumanga mwana wa nkhosayo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamumanga mwana wa nkhosayo ndi nyanga zake?
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti alandire msembe yabwino kwambiri m'malo mwa Isaki.

-Mwana wa nkhosayo anakakhala kuti sanamangidwe m'mutu kapena m'miyendo mwake, anakazipweteka poyesayesa kudzipulumutsa yekha.

-Mulungu ndi wabwino kwambiri.
-Mulungu adzalandira msembe yokhayo imene yili yabwino kwambiri.

-Abulahamu anamumasula Isaki ndikukamanga kamwana ka nkhosa kamene Mulungu anakapereka pa malo operekera msembe aja.

-Abulahamu anapereka msembe ya mwana wa nkhosa m'malo mwa Isaki.

-Mwana wa nkhosa anafa m'malo mwa Isaki.
-Mwana wa nkhosa analowa m'malo mwa Isaki.

-Kodi Abulahamu anaŵatcha kuti chiyani malo amene Mulungu anaperekera mwana wa nkhosa wa mphongo aja?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 22:14-19

14-Abulahamu anaŵatcha malowo kuti AMBUYE adzapatsa. Ndipo mpaka lero lino anthu amati, " Pa phiri la AMBUYE adzapatsa."

15-Mngelo wa AMBUYE uja anamuyitana Abulahamu kachiŵiri kuchokera kumwamba

16-ndipo anati, "AMBUYE akuti, "Ndikulumbira kuti ndidzakudalitsa kwambiri iwe chifukwa chakuti wachita zimenezi, osandimana mwana wako m'modzi yekha uja,

17-Ndidzakudalitsa ndipo ndidzakupatsa zidzukulu zochuluka ngati nyenyezi za kumwamba, kapenanso ngati mchenga wa m'bali mwa nyanja. Zidzukulu zakozo zidzagonjetsa adani awo onse,

18-ndipo mitundu yonse ya pa dziko la pansi idzalandira madalitso kudzera mwa zidzukulu zako, chifukwa chakuti iwe wandimvera."

19-Kenako Abulahamu anabwerera kumene anaŵasiya antchito ake kuja, Ndipo onsewo anapita ku Beereseba. Chomcho Abulahamu anakakhazikika komweko.

-Abulahamu anaŵatcha malo amene Mulungu anaperekera mwana wa nkhosa uja kuti, "AMBUYE adzapereka."

-Kodi chifukwa chiyani Abulahamu anaŵatcha malowo kuti, "AMBUYE adzapereka?"

-Abulahamu amkakhulupilira kuti tsiku lina Mulungu adzapereka Mpulumutsi kudzaŵapulumutsa anthu ngati m'mene Iye anaperekera mwana wa nkhosa kudzamupulumutsa Isaki.